







Ganizo

-  Ursula Nafula
-  Vusi Malindi
-  David Sani Mwanza
-  2
-  Chichewa ny



Mudzi wanga unali ndi mavuto ambiri.
Tinapanga mnyolo omozi kufuna kutunga
madzi.



Tinayembekezera zakudya zopasiwa ndi ena.



Tinakhoma manyumba anthu mwamsanga
chifukwa choopa akawalala.



Ana ambiri analeka sukulu.



Atsikana anasewenza maganyu m'midzi ina.



Anyamata anali kuyendayenda mumidzi ina ndipo ena anali kuchita ganyu m'minda ya ena.



Pamene mphepo yakuntha, mapepala opanda nchito anakhalila pa mitengo ndi mipanda.



Anthu anadulidwa ndi magalasi oonongeka
amane anataidwa mosasamala.



Ndipo tsiku lina, pompi inauma ndipo madzi anatha.



Atate anga anayenda khomo ndi khomo
kupempha anthu kuti apite ku msonkhano wa
m'mudzi.



Anthu anasonkhana pansi pa mtengo ukulu ndipo anamvesera.



Atate anga anaima nati, “Tifunika kusewenzera pamozi kuti tithese mavuto athu.”



Wa zaka zisanu ndi zitanu, Juma, omwe anakhala ma nthambi ya mtengo anakuwa nati “Ndingathandize ndi kusesa”.



Mzimai umozi anati “azimai angasewenze pamozi ndi ine kuti tibyale zakudya.”



Bambo wina anaimilila nati “Amuna azakumba chisime.”



Tonse tinakuwa ndi mau amazi ndikuti, “
tifunika kusintha myoyo yathu.” Kuchoka pa
tsiku lija, tinasewenzera pamozi kuthesa
mavuto athu.



Global Storybooks

globalstorybooks.net

Ganizo

 Ursula Nafula

 Vusi Malindi

 David Sani Mwanza

